# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

**Za kupita ku calichi**

1. Zifukwa za kupita ku calichi
2. Momwe tipembedza Mulungu m'calichi
3. Kubweretsa anthu ena ku calichi

Nalemekeza Mulungu, ndi kukhala naco cisomo ndi anthu onse. Ndipo Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumutsidwe. Macitidwe a Atumwi 2.47

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

- ©Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

**1. Zifukwa za kupita ku calichi**

*Pomwepo udzakondwa mwa Yehova – Yesaya 58.14a*

**Kuwerenga**
Mateyu 28.1-8

**Malongosoledwe**
Kodi Mulungu anagwira nchito masiku angati polenga kumwamba, dziko lapansi ndi cilengedwe cina conse cotizungulira? Inde, anagwira nchito masiku asanu ndi limodzi. Anapanga mitengo ndi zomera zina zonse, mbalame ndi nyama zina zonse ndipo pomalizira Iye analenga anthu. Analenga zonse m'masiku asanu ndi limodzi. Kenaka panali tsiku lacisanu ndi ciwiri. Nchito zonse za Mulungu zidamalizira. Ndipo pa tsiku lacisanu ndi ciwiri, Mulungu anapuma. Anapuma nasangalala kuona zonse zolengedwa ndi Iye.
Kodi mukumbukira phunziro la kulengedwa kwa anthu? Kuti Mulungu analenga anthu m'cifaniziro cake? Anthu analengedwa kuzikhala monga Mulungu. Cifukwa cake Mulungu afuna anthu kukhala ndi tsiku lopuma, cimodzimodzi monga Mulungu anakhala ndi tsiku lopuma. Ndipo tsiku limenelo ndi tsiku la anthu kuti asangalale m'zonse zimene Mulungu awacitira.
Mulungu anacha tsiku iri lopuma kuti 'tsiku la Sabata'. Ndipo tsiku iri ndi lofunikira kwambiri kotero kuti m'malamulo ake, Mulungu anapatsa lamulo lokhudza tsiku iri. Lamulo iri likamba kuti, 'Uzikumbukila tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza nchito zako zonse; koma tsiku lacisanu ndi ciwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako'.
Tsiku iri lopuma litipindulitsa. Mulungu sanatope atalenga kumwamba, dziko lapansi ndi zina zonse, koma *ife* tilema pamene tigwira nchito molimba. Ngati tiribe tsiku lopuma, tidzatopa kwambiri. Mulungu adziwa kuti tifunika tsiku lopuma. Anaticitira bwino pamene anatiuza kupumula tsiku limodzi pa sabata lirilonse.
Koma citanthauzo ca tsiku lathu la Sabata ndi cacikulu cuposa ca kukhala tsiku lopuma cabe. Ndi tsiku losangalatsa. Ndi tsiku loganizira Mulungu ndi kukhala osangalala pa zonse zimene atipatsa ndi kuticitira. Tsiku la Sabata liyenera kukhala tsiku lokondweretsa kwambiri la kulemekeza Mulungu.
Tsiku lathu la Sabata litanthauza cinthu cina copambana. Mulungu atiuza kuti pa tsiku la Sabata tizikumbukira lonjezo lake. Mulungu analonjeza kutipatsa Sabata lina: Sabata labwino kuposa. Sabata ilo ndi lamuyaya. Sabata ilo lodabwitsa lidzabwera potsiriza nthawi, pamene adzatenga anthu ake onse naye ku ulemerero wake. Pa nthawi iyo nchito zathu zonse zobvuta zidzatsira. Ndipo tidzasangalalira Mulungu mpaka muyaya. Sabata ilo lodabwitsa lidzakhala Kumwamba.
M'miyoyo yathu, tsiku lathu la Sabata (tsiku lopuma) ndilo pa tsiku la Sondo. Tilicha tsiku iri 'tsiku la Ambuye', pakuti Ambuye Yesu anaticitira zodabwitsa makamaka pa tsiku ilo. Pa tsiku la Sondo, Yesu anauka kwa akufa. Pa tsiku la Sondo, Yesu anatuma Mzimu Woyera kukhala m'mitima ya anthu ake. Cifukwa cake pa tsiku la Sondo timapita ku calichi kulemekeza Mulungu, kumpembedza ndi kumvera Mau ake. Tsiku ilo ndi tsiku lokondweretsa.
Anthu a kale a Mulungu anaiwala kuyeretsa tsiku la Sabata nthawi zina. Anaiwala kulipangitsa kukhala tsiku la Mulungu. Iwo anangokhala ndi nthawi yabwino pa tsiku limenelo. Anapangitsa tsiku ilo kukhala tsiku lokondweretsa iwo okha. Anasowa cisangalalo mwa Ambuye. Yesaya mneneri wamkulu, anawauza kuti azilemekeza *Ambuye* pa tsiku lake.

**Kukambirana**
1. Kodi cifukwa coyamba ca kupita ku calichi pa tsiku la Sondo ndico ciani?
2. Kodi cifukwa caciwiri ca kupita ku calichi pa tsiku la Sondo ndico ciani?
3. Kodi cifukwa cacitatu ca kupita ku calichi pa tsiku la Sondo ndico ciani?
4. Anthu onse a Mulungu adzakhala naye Kumwamba ndi kukhala okondwera mwa Ambuye mpaka muyaya. Nanga inu, ndinu m'modzi wa anthu ake?
5. Kodi mumayeretsa bwanji tsiku la Mulungu?
6. Kodi tingathandizane bwanji kuyeretsa tsiku la Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Tikuyamikani Mulungu wa Kumwambamwamba, kuti mutipatsa tsiku la Sondo kukumbukira nchito zanu zazikulu. Tsiku lanu ndi tsiku lokondweretsa ndithu. Mutithandize kuyeretsa tsiku lanu ndi kukulemekezani m'miyoyo yathu yonse. M'dzina la Yesu Mpulumutsi tikupemphani izi. Amen.

## 2. Momwe tipembedza Mulungu m'calichi

Ambuye Yesu ananena:
*Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao – Mateyu 18.20*

**Kuwerenga**
Salimo 122

**Malongosoledwe**
Pa tsiku la Sondo timabvala zobvala zooneka bwino koposa. Ndife osambika bwino. Tioneka aukhondo ndi abwino. Kenaka tipita ku calichi.
Ndi cifukwa ciani timabvala zobvala zooneka bwino koposa pa tsiku la Sondo? Ndi cifukwa ciani timasamba bwino kwambiri? Ndipo ndi cifukwa ciani timapita ku calichi?
Tingapembedze Mulungu kunyumba. Tingakhala okondwera mwa Ambuye pa tsiku la Sondo. Koma tipita ku calichi kupembeza Mulungu kumeneko. Mulungu anatiuza kuti akondwera pamene tisonkhana m'nyumba yake kumpembedza. Ndipo analonjeza kukhala nafe *kumeneko*. Indedi, timabvala zobvala zathu zooneka bwino koposa pamene tipita kukomana naye. Baibulo litiuza kuti tidzabvala zobvala zoyera ndi zooneka bwino pa nthawi ya nthawi ya Sabata la muyaya, pamene tidzalemekeza Mulungu m'ulemerero nthawi zonse. Zobvala izo zionetsa kuti macimo athu onse anacotsedwa.
Kodi timapembedza bwanji Mulungu m'calichi? Timlemekeza mwa kukhala zii. Tifuna kukhala zii kuti tikhoza kuganizira za Iye ndi nchito zake zodabwitsa, makamaka nchito yake ya cipulumutso. Ndipo timapembedza Mulungu mwa kumuimbira nyimbo. Ndipo timampembeza mwa kupemphera. Tipemphera mosamveka, m'mitima yathu, aliyense pa yekha. Komanso tipemphera pamodzi, pamene abusa alankhula ndi Mulungu.
Timapembezanso Mulungu mopereka ndalama zathu. Mulungu adzagwiritsa nchito ndalama zathu. Agwiritsa nchito ndalama zathu kuthandiza anthu ena. Agwiritsa nchito ndalama zathu kutuma atumiki kuti iwo auze nthano za Yesu kwa anthu amene sadziwa Mulungu. Ndife okondwera kupatsa Mulungu ndalama zathu, pakuti timkonda.
Ndipo timapembedza Mulungu mwa kumvera zimene atiuza. *Iye* alankhula nafe pamene abusa awerenga Baibulo ndiponso pamene abusa afotokoza Baibulo. Abusa atiuza za Mulungu ndi Ufumu wake wodabwitsa wa Kumwamba. Atiuza m'mene Mulungu afuna ife kumukhulupirira ndi kumvera. Ngati timvera Mau a Mulungu (Baibulo) ndi kuwatenga m'mitima yathu, Mulungu akondwa ndipo adzatidalitsa. Pamene tapembedza Mulungu moonadi, tibwerera kunyumba mosangalala.
Tsiku limodzi, pamene Yesu anali Mnyamata, Iye anapita ku Kacisi. Anakonda Kacisi cifukwa Kacisi unali Nyumba ya Atate wake. M'Kacisi Yesu anapeza amuna amene anakonda kulankhula za Yesu. Yesu anamvera. Anafuna kuwamvera kulankhula za Atate wake wa Kumwamba, cifukwa Iye anakonda Atate ake kwambiri. Yesu anamvera nafunsa mafunso nthawi zina. Ndipo anaiwala kupita kunyumba! Patapita nthawi, tate wake ndi mai wake anabwera kumtenga. Iwo anadabwa poona kuti Yesu anali kulankhula ndi amunawo anzeru!
Ife tiyenera kufuna kuphunzira zonse za Mulungu. Iye ndi wodabwitsa!
Pamene tipita ku calichi, tiyenera kumvera bwino kwambiri. Tiyenera kuimba ndi kupemphera. Tiyenera kuganizira Yesu ndi cikondi cake ca ife.

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani mumapita ku calichi?
2. Kodi tingapembedze bwanji Mulungu m'calichi? Patsani mayankho asanu.
3. Kodi Mulungu aticitira ciani m'calichi?
4. Kodi mukonda kupita ku calichi? Ndi cifukwa ciani mwayankha tero?
5. Kodi mukumva bwanji za anthu amene sapita ku calichi cifukwa ca mphepo, mvula, nchito kapena kulandira alendo? Tingawayankhe bwanji?
6. Kodi tingalimbikitsane bwanji kupita ku calichi?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu tikuyamikani kuti mumatipatsa mpata kupita ku calichi mwaufulu. Mutithandize kumvera ndi kumvetsa Mau anu. Muthandizenso abusa kuzimasulira bwino Baibulo. Mutiphunzitse kukhala osangalala mwa Inu nokha. M'dzina la Yesu Kristu, mwa cisomo takupamphani izi. Amen.

**3. Kubweretsa anthu ena ku calichi**

*Ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate – Afilipi 2.11*

**Kuwerenga**
Yohane 1.44-51

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira zimene Yesu ananena Iye asanapite Kumwamba? Anauza ophunzira ake kupita kulikonse ndi kuuza mitundu yonse za Iye.
Ngati ndife okondwera mwa Yesu, tifuna anthu enanso kukondwera mwa Iye. Ngati ndife okondwera kupembeza Mulungu m'calichi, tidzafuna anthu enanso kubwera nafe kupembedza Mulungu.
Andreya ndi Yohane anali ophunzira oyamba a Yesu. Tsiku lina analondola Yesu amene Iye anali kuyenda pafupi ndi mtsinje. Pamene Yesu anawaona, Iye anawaitana kubwera naye kunyumba kwake. Tsiku limenelo Yesu analankhula nao za Ufumu wa Kumwamba.
Andreya ndi Yohane anamvera mosamalira! Iwo sadamve uthenga wodabwitsa wotere nthawi zonse. Iwo sadamve Munthu wodabwitsa wotere!
Pamene Andreya ndi Yohane anapita kunyumba, Andreya anafulumira kupeza mbale wake Simoni.
'Simoni', iye ananena, 'tapeza Kristu!'
Kristu? Simoni analephera kukhulupirira kuti Andreya adapeza Kristu. Zaka zambirimbiri anthu a Israyeli adayembekezera Kristu kubwera. Ndipo tsono, mwadzidzidzi, Andreya ananena, 'Tampeza!'
Pamene Simoni sanakhoze kukhulupirira, Andreya ananena, 'Bwerani. Ndidzakuperekani kwa Iye!'
Simoni anayenda ndi Andreya ndipo anamva Yesu kulankhula za Mulungu ndi Ufumu wake. Kenaka iyenso anakhulupirira kuti Yesu ndi Kristu.
Simoni anakondwera kuti Andreya adamuuza za Yesu nakumperekeza kwa Iye. Iwo, Andreya ndi Simoni, komanso Yohane, anasandulika ophunzira a Yesu.
Ngati *ife* tidziwa Yesu ndi kumkonda, tifuna anthu enanso kumdziwa. Mulungu anatipangitsa kukhala okondwera potionetsa cikondi cake ca ife. Ndipo tifuna anthu ena kukondweranso mwa Yesu. Iye ndi Munthu waukulu wopambana.
Komanso, aliyense azikonda Yesu. Aliyense azikonda ndi kupembedza Mulungu ndi kumumvera. Tinalengedwa cifukwa ca Iye, kuti tizimkondweretsa. Anthu amene sakonda Yesu, sakondweretsa Mulungu. Tifuna iwo kubwera ku calichi kuti aphunzire za Mulungu ndi momwe azikhala miyoyo yao kwa Mulungu.

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani Mulungu afuna kuti aliyense azimpembedza?
2. Kodi Andreya anacita ciani kuti Simoni adziwenso Yesu Kristu?
3. Nanga inu, mumacita ciani kuti anthu ena adziwe Yesu Kristu?
4. Ndi cifukwa ciani kudziwa Yesu ndi cinthu cotikondweretsa?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Anthu onse ayenera kukutumikirani. Inu ndinu Mlengi wathu wamkulu ndi woyera. Munatilenga ku ulemerero wanu. Nthawi zambiri tilakwa ndi kucimwa. Nthawi zambiri tifuna cabe kudzikondweretsa m'malo mwa kukukondweretsani. Mutikhululukire chimo liri ndiponso macimo ena onse. Tipatseni Mzimu wanu mwa cisomo, kuti tikhale atumiki athu amene afalitsa uthenga wabwino wa Yesu Mpulumutsi. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu, Amen.